

## Chikhulipiro

Chinthu choyamba ndifuna kufunsa inu amene mukuwerenga uthengawu, kodi ndinu mkristu? Mkristu kutanthauza kukhala ndi moyo monga wa Yesu Kristu. Kodi m'moyo wanu mumachita zinthu zomwe Yesu Kristu anachita m'moyo wake? Anayenda-yenda nachita zabwino, nachirtsu wonse wosautsidwa ndi mdierekezi.

Kodi gwero ndi cholina cha moyo wanu ndi chiyani? Ndichofunika kwambiri kuti cholina chanu chikhale chabwino; kapena mu kuchita chinthu cholakwika, ngakhale chikuoneka ngati ndi chabwino? Kodi cholina chanu ndikukhala ndi nyumba, kapena kukhala ndi galimoto pamodzi ndi ndalamu Banki, kaya mufuna kukhala ndi Bizinezi, kutamidwa, kutchuka, kapena mphamvu mu dziko lino? Bwenzi langa awa ndi masomphenya achabe. Ngati munali wolemera kwambiri, wotchukitsitsa, munthu wa mphamvu zambiri mu dziko, zonsezi ndi zachabe ndipo ndikungosautsa mzimu. Mfumu Solomoni wa m'Baibulo, anali ndi zinthu zonsezi, koma anazitcha zachabe.

Kuoneka munthu wolungama kwa Mulungu ndiye cinthu chimodzi chokondweretsa ndiponso chabwino chotifikitsa kumoyo weni-weni. Kukhala wophunzira kufika patali kulingana ndi maphunziro a masiku ano, zonsezi m'moyo wako, ziribe phindu; pakuti zinthu zonse za mdziko lino zidzaonongeka panyengo yochepta, ndiponso sikudzakhala chikumbutso cha zinthu ziri zonse za mdziko.

Ngati tinena zokonzekera za mtsogolo, nanga tsogolo ndi liti? Kodi siliri ndi Mulungu? Mulungu asunga mtima wa mfumu mdzanja lache auloza komwe afuna ngati mtsinge wa madzi, Bukhu Lopatulika litiuza. Apanga chabwino ndi choipa ndiponso njira yache ili mu zinthu zonsezi, kulingana ndi mau a Mulungu.

Kulibe za mtsogolo mdziko lino mgakhale mdziko lirinkudza, kopanda Mulungu. Ndinalankhula ndi mtsogoleri wina nthawi yina pa zamtsogolo m'moyo wache. Iye anali kuganiza zakumtumikira Mulungu atatsiriza kulipira ndalamu za nyumba yache, koma pa nthawi imene analipira ndalamu zache zotsiriza, mwana wache m'modzi anafera pa nyanja kuseli kwa nyumba yache. Zikanakhala bwino akanadzipereka kwa Mulungu pa chiyambi.

Munthu wina anabwera pa musonkhano wathu tsiku lina; ndipo pamene mzimu wa Mulungu unali kuyitana anthu kuti alape, munthuyo anapatsidwa nthawi yakuti alandire chipulumutso, koma anakana. M'mawa mwache pafupi nafe, m'nyumba yamaliro nthawi ya masana ndinagany'ana nkhopre ya munthuyo wakufa m'bokosi. Imfa inamupeza mosachedwa atakana Mulungu. Iye sanakonzekere za kutsogolo.

Pa msonkhano wina, ndinauza amuna awiri ndiponso sanamvere. Pasanapite nthawi onse awiri anamwalira. Zingatitengere malo akuru kukamba zinthu zimene zachitira anzanga, zoonetsa kuti kulibe zamtsogolo kwaife ngati tribe Mulungu.

Kulibe mtendere kwa oipa, Bukhu Lopatulika litiuza. Mumveka zoopsyetsa m'makutu mwa anthu wolemera zakuti sizitha kuleka. Kukhala wodwala mopitilira pa mulandu wakuopa imfa yawokondedwa, kusokezeka ndiponso kupitilira kwa mabvuto m'makhalidwe kulebe phindu. Kubvitika ndiponso kuyesa mwamphamvu kupewa mabvuto wosowa ndalamu kapena kuopa kubedwa kwa katundu amene tamagwilira nchito, ndiponso kusasunga bwino anzathu munjira yopanda kumvetsa zobvuta zao, uwa siumoyo wabwino. Umoyo wodziwa mau a Mulungu koma wosatsatira, kudzinamiza ife tokha masiku wonse, pa mulandu wofuna kuganiza za m'mutu mwathu, kutsimikiza kwa ife tokha pa chikhulupiliro chosachokera m'mitima yathu. Kodi umenewu nkutchchedwa umoyo wabwino?

Cholina chathu chofikira patali panchito ya anthu anzathu chiyenera kukhala chimodzi cha zinthu zopanda bodza kapena kudzinamiza, ndiponso makhalidwe athu ayenera kukhala anzeru zabwino, masiku onse kukhala woganizira za masungidwe a abale athu. Aliyense waife ali wodalira wina ndi nzache kulingana ndi nchito zathu kwa wina ndi mzache. Mulungu anatipanga mnjira yotere; choncho ndife asungi a abale athu. Kaini anapha Abele ndiponso anakana kuti simsungi wa m'bale wache, pa mulandu wa chinyengo chache. Mulungu adzapatsa mphatso kwa munthu aliyense kulingana ndi m'mene munthuyo aliri. Iye amene asonkhanitsa chuma, koma mosalungama; pakati pa masiku ake chimdzasiya iye, ndipo pa chitsiriziro adzakhala wopusa, Mau a Mulungu atiuza motere.

Musakhale wofuna nyumba zabwino chabe, ngakhale magalimoto ndi zina zotere zimene anzanu ali nazo. Musaganize zopatsidwa ulemu, kapena kudziwika, kapenanso kukhala ndi udindo m'moyo wa dziko lino chabe, koma muganize za zipatala za anthu wofuntha (amisala) ndiponso zipatala za anthu a zifuwa, ndi zapatala za matenda wosiyana-siyana ndiponso muziwerenga nkhani za m'mapepala ndi ngozi za umoyo uno, kulingana ndi zomwe mumvera likiti-likiti m'matauni akulu monga kulira kwa chenjezo loopsya (alarm). Izi zinthu zoopsy ndiponso zonama zomwe zipatsa mantha ndi kusamvana, zindidziwatsa ine kuti uwu sindiye umoyo. Kuli m'malo m'mwamba wokhalamo komwe kuli chikondwerero, mtendere ndi chilungamo. Kumtumikira Mulungu kubwere tsa zonsezi.

Liwu lodandaulira limene lakhala likuyitana mu zaka zonse zakumbuyo, likuyitananso iwe ndi ine. Ndi liwu la Mulungu, kopyolera munthito za Mulungu ndi ana a Mulungu, kudandaulira anthu kuchokera pachiyambi cha dziko.

Mawa awa a Yesu Kristu analankhulidwa m'mibadw yapisayi. Analankhulidwa pa nthawi ya Nowa lisanafike tsiku lachionongelo. Analankhulidwa m'masiku a Yesu Kristu pomwe ngozi isanachitike mu Yerusalem. Anakombidwanso ku anthu amthengo, wofuna kubisala kumabvuto a moyo uno, mukupambana kwao kwabvuto m'masiku apita mumbiri ya zaka zakumbuyo. Kuchokera kale umoyo wabwino umveka ndi wa munthu wa kuGalileya amene anakhala yekha, anakhala umoyo wobvutika pa mulandu wa iwe ndi ine. Tsiku lalero liwu ili likulankhula, kulankhula kwakulu kwa anthu adziklonse; ndikufunsa funso, "M'bale wanga, Kodi chifukwa ninji sufuna kumvera kuyitana uku kwa kuti ulape, ndi kuchoka ku makhalidwe a umoyo uyu?" Kuti uphatikane nawo wodzichepetsa.

Kristu ananena nati; m'badwo wotsiriza udzakhala waliuma, wolimbirira, wotukumuka mtima, ndiponso wokonda zokondweretsa munthu, osati wokonda Mulungu; Paulo ananena nati awa ndiwo anthu amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. Ambiri a inu amene ndakukambani muli kale owtchedwa ndi zisulo ku nzeru zanu ndiponso kuganiza kunatha pokhala kuti munadzipereka, kwa mzimu wa Satana, kwakuti muchita zinthu zosakondweretsa Mulungu.

Poona kuti zinthu zonse zidzaonongeka ndiponso kuti dziko lonse, lidzaotchedwa Petro anafunsa, "Kotero tuyenera inu kukhala anthu wotani nanga, m'mayendedwe wopatulika m'chipembedzo," akuyembekezera ndikufulumira kwa kudza kwache kwa tsiku la Mulungu.